UNDUNA WA ZACHILENGEDWE

NTHAMBI ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NYENGO MSABATAYI

Yatulutsidwa : 08 November 2026 | Kuyambira pa 9 mpaka 15 November, 2026

NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

M'sabatayi, tiyembekezere mvula m'madera ochulukirapo m'chigawo cha kumpoto ndi m'chigawo cha pakati kuyelekeza ndi m'chigawo cha kum'mwera (Chithunzi 1). Nyengo yotentha kwambiri ipitilira m'madera ambiri.

Lolemba mpaka Lachitatu, kudzakhala mitambo yapatalipatali, mvula ya mabingu m'madera ochepa, ndi mphepo ya mphamvu m'madera ena. Izi zikhala chonchi kamba ka mkumano wa mphepo zochokera kumpoto cha kumvuma komanso zina zochokera kumwera cha kumvuma.

Kuyambira Lachinayi, dera la mpweya opepuka (lomwe likuyembekezeka kubuka ku Mozambique Channel) lidzalimbikitsa mvula ya mabingu m'madera ambiri makamaka m'chigawo cha kumpoto, madera a m'bali mwa nyanja ya Malawi, ndi madera ena a m'chigawo chapakati. Mvula ya mabinguyi ingadzathe kugwanso m'madera ochepa a m'chigawo cha kumwera.

Mwera wa mphamvu akuyembekezeka pa nyanja choncho asodzi ndi ena onse ogwiritsa ntchito nyanja akhale osamala.



Chithunzi 1: *Ulosi wa mlingo wa mvula m'sabata ikubwerayi*

NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunali nyengo yotentha m'madera ambiri komanso mvula ya mabingu m'madera ochepa amdziko muno. Komwe inagwa yochuluka kwambiri kunali ku Chileka ku Blantyre ndi mlingo wa 44.4mm pa 5 November komanso ku Mbawa ku Mzimba ndi mlingo wa 29.6mm pa 4 November.

Komwe kunatentha kwambiri ndi kwa Ngabu ku Chikwawa ndi **42.9°C** pa 8 November 2026. M'madera ambiri kunatentha kudutsa mlingo wokhazikika wa November. Kwa Ngabu kunatentha kudutsa mlingo wokhazikika ndi **5.8°C** (Chithunzi 2)

Malo otsindikizira: Blantyre

For further information, contact: The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services P.O. Box 1808, Blantyre. Tel: +265 991 69 00 61, Email: metdept@metmalawi.gov.mw X: https://x.com/MetMalawi, WhatsApp channel: Department of Climate Change and Meteorological Services, Web: www.metmalawi.gov.mw, Facebook: Department of Climate Change and Meteorological Services.

For area specific forecast, please download Zanyengo App on Play Store.

UNDUNA WA ZACHILENGEDWE

NTHAMBI ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO



Chithunzi 2: *Mlingo wakatenthedwe poyerekeza ndi kutentha kwa nthawi yayitali*

MALANGIZO M'SABATAYI

- Pamene kukutentha kwambiri sabata ino, tizimwa madzi pafupipafupi
- Tipewe kukhala padzuwa kwa nthawi yaitali, makamaka masana pamene kwatentha kwambiri.
- Pewani kusodza, kusambira kapena kugwiritsa ntchito mabwato ang'onoang'ono pamene mphepo ya Mwera ikuomba mwamphamvu.

Malo otsindikizira: Blantyre

For further information, contact: The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services P.O. Box 1808, Blantyre. Tel: +265 991 69 00 61, Email: metdept@metmalawi.gov.mw X: https://x.com/MetMalawi, WhatsApp channel: Department of Climate Change and Meteorological Services, Web: www.metmalawi.gov.mw, Facebook**:** Department of Climate Change and Meteorological Services

For area specific forecast, please download Zanyengo App on Play Store.